Mulungu anapereka mwana wake Yesu kuchokera mu chikondi chozama kwa ife kuti apelekedwe monga ku uchimo mmalo mwathu.

Nsembe ya Kristu ndi kukhetsa kwa mwazi wake mmalo mwathu ndi chifundo cha Mulungu ndi kutisambitsa kwa miyoyo yathu ndi mmene njira mmene anatiphimba umaliseche wathu ndi kuchot-selatu chosalungama chathu ndi manyazi athu. Chinthuzi cha Ezekiel ndi choonekera motero. Onenetsani kuti Mulungu anati zofuna zathu zili ngati umaliseche ndi zopanda pache. Kupatula iye ndi chikondi chake. Alemekizeke Mulungu wathu potichitira chokoma, kutisamala kutisambitsa ndi kutimveka ife ndi mwazi wa mwana wake amene anamutumiza!

Mwachoncho pa nthawi zina, pa zaka zopitilira 6000 zapitazo Mulungu poswa zimene zinali kutsatilidwa pa chiyero chake monga zakhuzidwira ku mabvalidwe (monga ndi Yesaya ndi Hosea) anali kuonetsera chiweluzo chake! Mwa zonsezi, anali kufunabe mkala pakati (Kazembe) mu mbadwo umenewo kuti aphwanye tembele-ro monga Yesu anachita. Tembelero ndi limene lidamuphetsa iye pa mtengo (mtanda) kuonetsera chake kwa munthu wa uchimo, umaliseche wa Issaih sunali kuyesera pa kuchita. Tembelero limene linali kwa munthu koma kuonetsera mkwiyo wa woyera umene anali nawo.

Gawo Lachinai

Ndi lero?

Ndi zonse zimene taona mu malembo woyera zokhudzana ndi zamaliseche, zikukudza bwanji moyo wathu, munjira yooneka? Tiyeni tiganizire za zinthu zina zimene choona cha umaliseche utifikira ife pafupi ku nyumba zathu lero lino.

Kusambira Kunyanya

Sizoti ndi zololedwa, koma zimanenedwa ndi machitidwe a dziko lapansi kuti kubvala kofafana ndi kabudula wang'ono wamkati, ndi kumayenda, kusambira, kukhala, ndi kutambalala patsogolo pa anthu onse amene ali kufuna kuti akuonere. Timaonetse latu thupi lathu lonse pa mtunda lonse ndi kuonetsa thupi lathu kwa anthu onse kwa alendo angakhalenso kwa abwenzi. Ndipo takhulupirika popatsira zinthu zotere kw aana athu ndi kuwaphunzitsa kuti zili bwino kuti kusabvala bwino ndi kubvala kotere ngati ndi padziwe

kapenanso mbali mwa nyanja zonsezi zikuchitika mu dzina la kusangalala (kupumula) ndi kulimbikitsa matupi.

Ganizilani za izi zaka makumi asanu apitawo (50) zinali zobvuta kuonetsa matupi athu mu njira yotere ndi anthu osazindikira chabe amene amaganiza zotere motero kuyambilira kwa zaka zapitazo. Amayi ndi zobvala zosambira zowoneka kuyambira pakhosi ndi mchafu. Mabvalidwe otchedwa (Victorian) koma pang'ono ndi pang'ono kubyola mu nyumba zowulutsira mau ndi zamalonda. (satanani ndiye ochita zimenezi) nthumazi yathu ndiye zamizidwa ndi kusakhala ndi umulungu.

Bvalani motero pitani patsogolo ndipo bvulani angakhale ndi kabudula wa mkati wanu. Yendani, thamangani zungulirani poonetsera kwa anthu onse amene afuna kuti akuwoneni kuti maso akhute ndi zotere. Ndi zoipa kodi? “chabwino,” Mdani amati Mulungu sakudzidwa ndi izi ndi zabwino ndithu zongocheza, chonde taganizani kachiwiri tagula bodza ili kuchokera kwa mdani wa Mulungu kuti tikhoza kukhala osabvala ngati ndi kusambira chabe kunyanja, ndiye chipatso cha kukumbatira ndi kusasamala ndiye zotsatira za chilakolako cha maso nsanje, zakutha ndi mpikisano wa thupi ndi kuonongeka kwa umunthu, kwa ongoyamba uku ndi mayeso abwino kuti inu muganize zimene timati sikulakwa kuti mungaganize bwanji kuti muone kuti muli ndi munthu mu chobvala cha mkati ndi kapisholo pa gome la chakudya chanu. Pafupi ndi ine mu Restaurant kapena kuti onse olandira ndalama mu sitolo onse ali mu panti ndi makasitomala ndikuganiza kuti mukhumudwa ndi kuganiza kuti sizili bwino pamabvalidwe otere. Koma mumuike munthu wa mkati ndiye kenako ndi kumabvomeleza kuti ndi zabwino ndi zobvomeleza chifukwa? Bwanji ndi maganizo awiri otere. Mwina zili bwino ndi malo otero osati choncho ai? Ngati ndi bwino kuti anthu akuone uli mphempete mwa nyanja ndi chobvala cha mkati koma osati zabwino mu shopu kapena mu Restaurant ali maliseche, nanga chabwino mu nyumba ya charichi? Kodi mungakhale ndi ana anu muli bwino pa bwalo lochezera ndi alendo onse pamodzi ndi kukhala ndi mabvalidwe otere mu kabudula wa mkati? moteremo sichoncho ai. Chasintha chiani? ndi maganizo athu chabe amene asinthidwa.

Mdani watinamiza potiuza kuti zili bwino ku zinthu zina powonetsa thupi lathu pa maso pa anthu ndi kuti maso athu okopeke kwa amuna kapena mkazi amenewa kufuna kuona zonse. Kodi ndi zabwino zimenezi. Tinene zoono, zoono ndi izi palibe mwana wa Mulungu ali ndi kubvomelezedwa kubvala chobvala chimene chili chobvala cha mkati ndi kupita kumalo owonekera anthu. Choonde musalora ana anu kuti akule ndi kuti kusabvala bwino ndi zabvomelezeka pokhapo kuli munadzi pa mtunda pa nyanja. Ndizoonadi po zimapangitsa Yesu kukhala okwiya Luka 17, 1-2.

Zolengeza

Mbali ina ya maliseche ndi imene ili kumbali ya zolengeza malonda pawalesi mapepala monga zolengedwa za opanga zinthu zamalonda. Kuonetsa azimayi ali mu kabudula wamkati (chino-chino) zikwangwani zoonetsa maliseche. Zobvala zowonekera mkati kuika pathupi zothina zogwira thupi zopezeka mu masitolo apamwamba. Ana okuwona ndi abambo wonse kuona zotero: zathupi zimene tinapangitsa kukopa chilakolako cha amuna ndi kudzazitsa maso ana pazimene sanakayenera kuona. Panonso ndi chitsanzo cha zimene dziko labvomeleza kuti ndi zololedwa kudzera njira ya makono mu zolengedwa malonda) kuonetsa mitundu yowoneka bwino. Luso lapatali ndi kusindikiza pa mapepala ndi kuonetsa zamaliseche. Chabwino kodi ndi zabwino kuona mu News pepala. Zolengeza malonda kapena zamaliseche zolengeza. Mapepala okhomedwa mu gawo la zogulitsa zobvala. Kodi ndi zoono kuti zolaula zikhale zoikidwa kwa ulere ndi kuti zili bwino. Ndikuganiza kuti sichoncho wina onditsutsa angati ndi zolengeza chabe basi, taisiyani ndi choncho? Tikubvala mbeu ya mtundu wanji kwa ana athu mu maganizo awo ndi mmalingaliro awo? Kukwelezera mafuta amene amachita nkhondo ndi maganizo ndi malingaliro ndi mitima ya woyera mitima a Mulungu zisamachitike motero!

Nthawi Zina Zapadela

Chifukwa chiani nthawi yapadera? Zimene zimaloledwa kuti munthu abvale kabudula wa mkati kapenanso zopanda zomangira kumbuyo monga zobvala zonse zili. Paukwati, kapenanso pa mgonero ndikumachitika motero. Koma mwana wa mtsikana ukhale ndi T-Shirt yotegula kumbuyo kuwonetsa msana yonse ndi kumabwera ku charichi

kwanu.

Mukuganiza bwanji pa zoonetsa matupi mu machitidwe otere osati monga zikamayenera kukhalira? Kodi tikubvomereza kusabvala bwino (kusamvera 1Tim 2) chifukwa cha chikhaliidwe choikidwa ndi kukhakitsidwa ndi zopezekapo? Kodi siuchimo?

ZAKU CHIPATALA

Talingalirani za ntchito ya chipatala kutibvula zobvala za mkati, kapenanso kukwiya chobvala. Kodi sizinabweletse mabvuto kwa anzathu amene ali madotoro, madotolo ndi anamwino pamene ali ife. Hmmm chifukwa ali ndi chikalata chowabvomeleza pa chipupa ndiye kumaswa mtima wa Mulungu ndi kutibvula maliseche athu mu machitidwe otere. Pafupinso ndi alendo? Kodi tinagamiza kawiri za zimene kw aife tokha ndi kwa ana athu? Chifukwa chiani _____ tikuchita chotero kwa ena kwa munthu chifukwa cha udindo patsogolo pa dotoro kapena namwino ndi kumaloledwa kubvula pamaso pa Dotoro? Kodi tikuona kunama kumene ife talowamu.

Sitikuti tiwasale ma Dotoro koma ndi nzeru ndi kuganiza kuti ndikwabwino kupeza amene ali ofanana nawe? Ngakhalenso kukhala ndi zobvala ngati kungatheke kutero? Sichisankho chanu chotere, ntchito ya chipatala ndi ya anthu amene tinaitana kuti atithandize. Sikuti iwo ndi mabwana athu, kuti tingakhale patsogolo pawo pachili chonse chimene alankhula kapenanso abweletsa angoitanidwa kuti atithandize pa zinthu zina. Osabvula pamenepo Mulungu ndi Mulungu iwo simulungu ai zinthu zina ndi zotheka kuzipatutsa, monga kumalo kutumbulira munthu kumene sikuloledwa chobvala china chimene munthu amabvala. Koma kodi sityenera kudziwa kuti tisingule bodza limene limati maliseche ndi abwino limene lili mu ntchito ya zipatala? Sitingathe kukana bodza limene sitifuna kuti tifunse zamanyazi mu office ya Dotoro chifukwa kuti zonse zowonetsedwa kuti ndi za ntchito basi ndipo zili motero. Tiyeni tikhale ndi Mzimu ozindikira ndi tcheru pa zinthu zimenezi. Akunja ndi a kunja. Kaya amabvala motani mu machitidwe ai koma mau a Mulungu ali chikhaliire owona. Kodi timadziwa kuti ophunzira aku chipatala kuti amabvulidwa pamene ali kuphumzira za chipatala? Mu kuphunzira

kwa zachipatala ophunzira amafunsidwa kuti ayese anzake ophunzira ali maliseche! Ndizokanidwa zimenezi. Ndikwabwino kupita ku maphunziro otere ndi kukana mau a Mulungu? Kuyang'ana maliseche ndi cha manyazi ndipo ndi choipa chokanizidwa. Kulembedwa ntchito kwa madotoro ndi anamwino kumafunika kuti ayang'ane maliseche athu ena) kusambitsa odwala, (giving shots) kuwatum-bura, kuwayesa ndi zina zotero) tingatani kwa ife amene tagulidwa ndi mwazi wa mtengo wapatali wa Mulungu? Kodi chofunika kwa ife ndi chotani? Zosamalira zathu... ndi ulemu uli pa ife monga ansembe a Mulungu?

Chisunzo

Palinso chitsanzo china chimene kusabvala bwino kukuchitika tsiku ndi tsiku mu dziko la chisunzo. Mu dzina la chisudzo kaya ndi zolem-ba lembe zosema kaya ndi zoumba timalora zochititsa manyazi ndi zolaura kuti ndi zabwino ndi kubvomelezedwa. Timati ndizoyelekeza chabe. Dziko limati ndi zinthu zimene zimayeneredwa kutamandika. Kwa zaka zambiri azisunzo otchuka akala kukweza zolzura kuti ndi zabwino ndipo dziko limati zili bwino. Koma sizakhale choncho kwa na a Mulungu. Tatengedwa kuchokera ku ufumu wa mumtima ndi ulamuliro wa Satana ndi mabodza ake onama tiyeni tisinthike pokonzanso malingaliro athu. Zoumba zamaliseche ndi zololedwa kuonetsedwa angakhalenso mu malo a chipembedzo. Ndizoipa kuti zili kuloledwa mu maikidwe otere poterenso kwa anthu a Mulungu. Kodi sanati Mulungu kuti **maliseche ndi chamanyazi**.

Gawo Lachisanu

Kukongola Kofanana Ndi Mulungu

Monga Yerusalem, Mulungu kawiri kawiri amamunena iye ngati mfumukazi, mukazi, mukazi wokodzedwa kukwatiwa kwa mwamuna wake. iye ndiye mkazi wokongola wa Mulungu. Mkazi wokodzedwa kufikila Kristuyo. Ife ndife mkaziyo, anthu amene Mulungu akuwakaza. Ndi chinthu chofunikira kwambiri kuwona ulemelero wache. Ndipo kulemekeza kutenga chinthunzi thunzi chakuti ife ndife ayani.

Ndipo chifukwa chiyani ife tiyenera kukhala ndi mtima woyera kwa iye.

Estere ndi chinthunzi thunzi cha mkaziyo, kapena mpingo.

Ndipo iye adalera Hadasa, Ndiye Estere, mwana wamkazi wa Atate wace wang'ono, popeza iye analibe Atate kapena amai ndi namwaliyo anali ndi maonekedwe okoma, ndi wokongola. Ndipo atamwalira Atate wace ndi mai wace, Moredekai anamtenga akhale mwana wace.

Pofika tsono kulowa kwace kwa Estere mwana wa Abihaili, atate wang'ono wa Moredekai amene adadzitengera akhale mwana wace, kuti alowe kwa mfumu, sanafuna kanthu koma zonena Hege mdindo wa mfumu wosunga mkazi ndizo.

Ndipo mfumu yidamkonda Estere koposa akazi onse, nalandira iye ku ndi chifundo pamaso pace, koposa anamwali onse; motero anaika korona wachifumu pamutu pace, namuyesa mkazi wamkulu m'malo mwa Vasiti.

Estere 2:7,15,17

Uneneri wokhuzana ndi Kristu ndipo Ukwatibwi wace:

Mwa omveka anu muli ana akazi a mafumu. Ku dzanja la manja lanu aima mkazi wa mfumu wobvala golide wa ku ofira. Tamvera, mwana wamkaziwe, taona, tachera khutu lako. Uwalenso mtundu wako ndi nyumba ya atate wako. Potero mfumuyo adzakhumba kukoma kwako: pakuti ndiye Mbuye wako: ndipo iwe ungwadire iye. Ndipo mwana wamkazi wa turo adzafika nayo mphatso.

Acuma a mwa anthu adzapempha kudziwika nanu. Mwana wamkazi wa mfumu ngwa ulemero wonse mkati mwa nyumba: zobvala zace zopangidwa ndi golide. Adzamtogolera kw amfumu wobvala zamawanga mawanga:- anamwali azace omtsata adzafika nao kwa inu. Adzawasogorela ndi chimwemwe ndi kusekerera: Adzalowa m'nyumba ya mfumu.

Masalmo 45:9-15

Uneneri okhuzana ndi mkazi wa Mulungu, Anthu ake

Chifukw acha Ziyoni sindidzakhala chete ndi chifukwa cha Yerusalemu. Sindidzatuluka kufikira chilungamo chake chidzatuluka monga

*kuyera ndi chipulumutso chache monga nyali yoyaka ndipo amitundu adzaona chilungamo chako ndipo udzachedwa dzina latsopano limene mkamwa mwa Yehova mudzatchura. Iwe udzakhhalanso limene mkamwa mwa Yehova mudzatchura. Iwe udzakhhalanso korona wokongola mdzanja la Yehova, korona wachifumu mudzanja la Mulungu wako. Iwe sudzachedwanso wosiyidwa dziko lako silidzachedwanso bwinja koma iwe udzachedwa Hefiziba ndi dziko lako Beula. Pakuti Yehova akondwera mwa iwe ndipo dziko lako lidzakwatiwa. Pakuti monga mnyamata akwatira nambali momwemo ana ako amuna adzakwatiwa iwe ndi monga mkwati akondwera ndi mkwatibwi momwemo **Mulungu wako adzakondwera nawe.***

Yesaya 62: 1-5

Chifundo cha Paulo:

*Pakuti ndichita Nsanje pa inu ndi Nsanje ya Mulungu. Pakuti ndi-
napatsani ubwenzi mwamuna mmodzi kuti ndikalangize inu ngati namwali woyera mtima kwa Kristu.*

2 Akorinto 11:2

Bvumbulutso la Yohane:

Ndipo ndinamva ngati mau khamu lalikulu ngati mkokomo wa madzi ambiri ngati mau a mabingu olimba nizinena Aleluya: pakuti achita ufumu Ambuye Mulungu wathu wamphamvu zonse. Tikondwere tisekere ndipo tipatse ulemero kwa iye pakuti wadza ukwati wa mwana wa nkhusa ndipo mkazi wake wadzikonzera ndipo anapatsa iye abvale bafuta wonyezimira woti mbu, pakuti bafuta ndiye zolungama za oyera mtima. Nsaru za bafuta ndi makhalidwe olungama a woyera mtima.

Chibvumbulutso 19:6-8

Ndipo ndinaona mzinda woyerawo Yerusalem watsopano uli kutsika kumwamba kwa Mulungu wokonzeka ngati mkwati wokometsedwa mwamuna wache ndipo ndinamva mau akuru ochokera ku mpan-do wa chifumu pa anthu ake ndipo adzakhala ndi iwo pamodzi. Adzakhala anthu ake ndipo Mulungu mwani adzakhala ndi anthu ake ndikukhala Mulungu wawo.

Chibvumbulutso 21:2-3

Uneneri wa Ezekiel ukudzana ndi Mzinda woyera:

Ndipo ndinakusambitsa ndi madzi, inde ndinasuka, kukucotsera

mwazi wako ndikukudzodza mafuta, ndinakubvekanso ndi nsaru zophikapika ndi kukumveka nsapato za chikopa ca katumbu ndinakuzenenga nsaru ya bafuta ndi kukuphimba ndi nsaru yasilika. Ndinakukomeseraso zokometsera ndi kuika zigwinjiri mmanja mwako, ndi unyolo mkhosi mwako. Momwemo ndinaika zipini m'phuno mwako ndi maperere m'makutu mwako ndi korona wokongola pamutu pako, ndipo ndinadzikometsera ndi golidi ndi silica ndi yopika pika: unadya ufa wosalala ndi uchi ndi mafuta: ndipo unali wokongola woposa ndithu, ndipo unapindula pindula kufikira unasanduka mfumu. Ndi mbiri yako inabuka mwa amitundu chifukwa cha kukongola kwako. Pakuti ndiko kwangwiro mwa ulemelero wanga ndinaika pa iwe ati Ambuye Yehova. Ezekiel 16:9-14

Mulungu amapereka kukongola pa anthu ake, ndipo ife tikhale anthu otere, obvekadwa ndipo opangidwa kukhodzedwa kufikira kwake kwa mukwatibwi. Ngati Mulungu ndi kukodzedwa kwa okonedwa zoperkedwa za mtengo ndi zobvala zokongola. Iye wakunena ndi chifundo, iye wapereka pa anthu ake kuti ayenda muchilungamo. Monga ife tachipereka kwa Mzimu wake mwa ife. Ife tili ndi ulemu wa kuziwonera kukongola kwathu ndi kalirole lache ndi moyo. Ife tinalibe ndi mwai wokhala ndi kukongola kotere mwa ife tokha, koma Mulungu wathu wa m'kulu. Ndipo opulumutsa atipasa ife colowacho kuti ife tikhale “owala ngati nyenyezi kucdziko lonse la pansu, ngati tikugwira mawu a moyo.” (Afilipu 2:4-16) Iye atipasa ife kukongola kuti timangidwe. (Yesaya 61:3) kukongola kwathu kwa mukati wa moyo, umene wofanana ndi chipatso ca Mzimu oyera; “chikondi kusangalala cimwemwe Mtendere, kudekha, kukoma mtima. Chiletso Agalatiya 5:22 23. izi ndi zipatso za mkwatibwi monga takwatiwa, ndalonjeza ife tokha kukhala opanda chilema, usakhala mu za dziko lapansi ndi mdima wake.

Paulo analemba

Amuna inu kondani akazi anu, monganso Kristu anaconda Eklezia nazipeleka yekha mmalo mwache kuti akampatule atamuyeleza ndi kusambitsa madzi ndi mau kuti iye akadzikire yekha Eklezia wa ulemelero, wopanda banga kapena khwiya, kapena kanthu kotero komatu kuti akhale woyera ndi opanda chirema” Aefeso 5: 25-27

Tingakhale okondwa motani pokhala ndi kulandira masiku athu padziko kukonzekera opanda banga mkwatibwi okongola! ndi mdalitso waukulu ndi kudala polandira ndi kugwira ntchito ya Atate mmalo mwa mwana wake Yesu.

Zingakhale zotani zonsezi ndi mabvalidwe. Ndi chiyembekezo tikupeza kuyamika kuti ndi chiyero, opanda banga ndi kuima mu miyoyo yathu pakufunika Mulungu. Tikukhala ndi chuma cha mtengo wake mu zotengera za dziko lapansi lotchedwa matupi. Tili ndi mzimu wa Mulungu ngati tibadwa kuchokera kwa iye. Timasunga Mulungu wa kumwamba, mlengi padziko lapansi pamene tili mtupi lathu. Taonani zoterezi! Kodi izi sizingatsitsimutse mitima yathu pokhala ndi udindo ndi kanthu ndi chiyero! Pakuti matupi athu sali aife tokha koma ogulidwa ndi dipo sitingakhale ndi maganizo kuzisamalira tokha. Ndi tcheru pa nkhanu ya kubvala? Osati pa zimene timabvala koma limenenso timabvalira?

Monganso mkwatibwi yakonzekera kukongola opanda banga kwa mwamuna wake yekha. Anapangidwa chifukwa cha iye 1Akorinto 11:9) osati wa dziko lapansi kapena kwa zakutha. Pakuti talamulidwa kuti ukwati uyenera kulemekezedwa ndipo.

Ndipo pakama la ukwati payenera kukhala poyera (Ahebri 13:4) sizingakhale zabwino kuti matupi ndi maonekedwe kuti aonekedwe ndi munthu, mmodzi yekha amene ali mkazi wathu? Kodi simiyoyo ndi matupi athu ali mphatso yopelekedwa mu mkati mwa miyoyo yathu?

Pamene nkhanu ya mabvalidwe ibwera ena ngati, kodi sizabwino kuti mzimayi adzioneka bwino? Sizimene Mulungu anapeleka, inde Mulungu anapereka koma ndi kwa mwamuna yekha kwa iye yekha. Ngati mphatso ya iye yekha basi iye thupi la mkazi silili kwa iye yekha komanso kwa mwamuna 1 Akorinto 7:4 sili la dziko lapansi la abale ena ngakhalenso kwa iwe wekha kuti ungakhale ndi kutamanda wina ndi zopita.

Izi ndi zitsanzo za kuyera ndi kukongola kwa kuyankha kwa mkazi wokongola kwa okonedwa wake ngati mungaimilire nokha mu

moyo umene Mulungu anaonetsa mu chithunzichi moyo wanu udzaimba ndi kumwetulira kapenanso kulira pakukongola kwache.

Ndipo anauka Rabeka ndi anamwali ake nakwera pa ngamira natsata munthuyo mnyamata ndipo anamtenga Rabeka namuka.

Ndipo Isake anadzera njira ya Beerelahai-roi chifukwa kuti anakhala iye mdziko la kuwera. Ndipo Isake anaturuka kulingalira m'munda madzulo, ndipo anaturuka maso ake nayangana taona, ngamira zinali kudza. Ndipo Rabeka anaturuka maso ake anatsika pa ngamira. Ndipo anati kwa mnyamata, munthuyo ndani amene ayenda mmunda kukomana ndi ife?

Mnyamatayo ndipo anati, uyo ndi mbuyanga: chifukwa chake nadziphimba.

Mnyamatayo ndipo anamuuzza Isake zonse anazichita ndipo Isake anamlowetsa mkaziwo mhema wa amake Sara, natenga Rabeka nakhala iye mkazi wake, ndipo anamkonda iye ndipo Isake anathonzedwa mtima atafa amake. Genesis 24:61-66.

Mu Genesis 24. Abrahamu anatumikiza wantchito wake kupita kwawo kukapeza mkazi wa mwana wake Isake. Wantchitoyo anapita ku malo otchedwa Nahor ndipo anampeza Rebecca. Namwali, bunthu okongola.” (Vesi 16) wantchito analankhura ndi Atate ndi alongo ake Betula ndi Laban ndikufunsa kuti Rebecca akhale mkazi wa Isake. Anati, uyu ndi Rebecca mutengeni ndi kupita lorani iye akhale mkazi wa mwana wa bwana wanga, monga Ambuye walankhulira. Rebecca anabvomereza kupita ndi watchitoyo pamodzi ndi one.

Onetsetsa pa zimene Rebecca anachita anachita atamva kuti mwamuna wake anali mmunda. Pamene anamva izi anatsika pa bulu ndipo anatibveka yekha. Anali namwali wokongola ndipo pamene anamva kuti ndi Isake mwamuna wake watsogolo amene sanamuonepo adachita chiani? anabisa ulemero wake kukongola kwake. Kudikilira nthawi ndi malo kumene kukabvulidwe. Kuyankha kwake sikunali kukonza tsitsi lake ndi kuyamba kuseka. Ai, anazibveka yekha mukuzichepetsa ndi mwaubwino ndi ulemu.

Onani tsopano machitidwe amene mzimayiyo anayankha pokhala ndi maonekedwe abwino, kukongola ndi ulemero unapatsidwa, kwa iye. Mu Ezekiel analemba za mkazi ameneyu Yerusalemu.

Ndipo anadzikometsera ndi golidi, ndi siliva ndi chobvala chake ndi bafuta ndi silika ndi yopikapika. Unadza ufa usalala ndi uchi ndi mafuta ndipo unali wokongola woposa ndithu. Ndipo unapinndula – pindula kufikira unasanduka ufumu. Ndi mbiri yako inabuka mwa amitundu chifukwa cha kukongola kwako pakuti ndiko kwangwirowo mwa ulemelero wanga ndinauika pa iwe, ati Ambuye Yehova.

Ezekiel 16:13-14

Kukongola kwake kunali chifukwa kuti Mulungu anachita chonchochi kwa iye. Mulungu anampatsa kwa iye kukongola kwake kunali kwabwino chifukwa kunachokera ndi kudalitsa kwa Mulungu. Koma kuyankha ku dziko lapansi kunali koipitsa kukongola kwake ndipo anakhala wa chiwerewere yekha ndi anthu ena kuononga kuyera kwa iye ndi kwa mwamuna wake yekha osati kwa ena ai. Weren-gani pa zimene zimaoneka zinakhala pakukongola ndi maonekedwe abwino kuti ena awone.

Koma unatama kukongola kwako ndi kuchita zachigololo potama mbiri yako ndi kutsamulira zigololo zako pa munthu aliyense wopitapo unali wache! Ezekiel 16:15-16

Anatenga kukongola kumene Mulungu anapeleka ndi zobvala ndi kuzitambasula kwa abwenzi ena. Kwa ena onse odutsapo ndipo kukongola kwake kunakhala kwa iwo monga zinaliri, koma kuchokera kwa Mulungu ndi kwa iye yekha. Ndipo anapitiliza kukongola kwake kwa anthu ena aliyense amene anafuna. Zimenezi siziyenera kuchitika zisamachitike ai.

Kukongola kwathu ndi matupi athu anapelekedwa kwa amuna athu okha. Akazi ali ndi maonekedwe abwino powapenya, ndipo timadziwa mmene tingaonetsere zimenezi pamene tifuna kutero koma ndi uchimo. Ngati tionetsa mosakhala ndi chiyero ndipo ndi mphatso yosadetsedwa kw amwamuna. Sitikunena kuti tisamaonekedwe bwino kwa amuna athu ai. Koma ngati tisamala zotere

ndiye kuti mzimu wathu udzatsika chifukwa cha mabvalidwe athu. Ngati tang'amba kuti tidzionetsa makandatchembere musamachite ai. Ndipo ngati mukubisa thupi lanu ndi zopisa zopepera zongocho- kera pa khosi ndi mchiuno ndipo kuti mukadutsa malire otere. Ndi zotheka kubisa maliseche koma osati ulemelero.

Ndi ndani amene akufuna kubisa zosokedwa bwino ndi bwino kub- vala zomangidwa bwino ndi lamba? Sidziko limene limatiuza zo- khudzana kuonetsa mbali ina ya matupi athu. Tikayamba kusunga chuma chimene tapatsidwachi ndi chimodzi chokhachi chapeleked- wa ndi cholinga chotere. Ndidzapeza mtendere ndithu. Tikapeza mtima wathu pamodzi ndi mosungilamo katundu wathu. Mulungu adzatitsogolera ndi mzimu wake pa zimene zili zabwino ndi kub- vomelezedwa ndi mabvalidwe abwino ndi kumasulira kwache ndi kuti tikhale tcheru posakhumudwitsa ena chifukwa cha matupi athu amene ali kwa Kristu ndi amuna athu okha.

Pamene tikuyesa mitma yathu tizifunsenso kuti tikubvala ichi pa chifukwa chotani? Kodi pali gawo lonyada kuchokera mu malaya amene tabvalayo. Kodi tikufuna kuti paonekere pali ponse kwa anthu? Ngati ndife amuna kodi pali kunyada ndi kukula kwa thupi lathu.

Timakonda kuwonetsa kwa miyendo yathu ndi kukwezera kabudu- la, muwamba kuti tionetse miendo. Tili ndi zofuna kuonetsa, phazi lokha kuti tiyende popanda nsapato mu njira yotere? Ndikumaone- ka bwino? Ganizani za zimenezi.

Ngati zina zabwino zimene zili za ife eni zimene ndizabwino chifuk- wa timazikonda ife eni tamukhumudwitsa Mulungu mtima wake ndi kuika Yesu pambali ndi yekhayo amene ali oyenera ndi kupam- bana ndi kuganizidwa bwino.

Tilore kuti zonse izi zitakase mozama potidziwitsa pa zofuna zathu kwa iye.